# MAWU A ANDUNA

## YA ZAMAGETSI

## OLEMEKEZEKA A ATUPELE AUSTIN MULUZI

## PA MWAMBO WOYATSA MAGETSI

## M'BOMA LA RUMPHI

## PA

## THAZIMA PRIMARY SCHOOL

## PA 1ST JUNE, 2020

- **Mlembi wamkulu wa Magetsi Bambo Joseph Mwandidya;**
- **Mtsogoleri Wamkulu wa Zamagetsi, Mai Chimwemwe Gloria Banda;**
- **Mkulu wa kampani yogawa magetsi (ESCOM);**
- **Mkulu wa kampani yopanga magetsi (EGENCO);**
- **Mkulu woona za mafuta mdziko muno (NOCMA);**
- **Mkulu wa Kampani yogulisa magetsi (PML);**
- **Bwana mkubwa wa boma lino, Bambo a Fred Movete.**
- **Paramount Chief Chikulamayembe ndi mafumu onse mwabwera pano.**
- **Olemekezeka aphungu nonse muli malo ano;**
- **Akuluakulu a Boma;**
- **Mamembala a Nyumba zofalitsa mau;**
- **Amayi ndi Abambo, anyamata ndi atsikana.**

***Mulibwanji Nonse!!!!!!!***

Alendo olemekezeka, amayi ndi abambo mwachidule nonse mwafika pano pa Thazima Primary Sukulu, ndikulandireni nonse ku mwambo woyatsa magetsiwu.

Boma limazindikila kuti magetsi ndi chinthu chofunika kwambiri pa moyo wa anthu onse kaya okhala kumudzi kaya okhala mutauni. Ndichifukwa chake lidakhazikisa ndondomeko lotchedwa MAREP imene imaika magetsi madera akumudzi komanso ma tauni ang'ono ang'ono. Izi zili chomwechi pofuna kuti nawonso anthu okhala ku maderawa azikhala ndi moyo wapamwamba. Ndipo boma lili pakalikiliki kuonetsetsa kuti ntchito imeneyi ikupita patsogolo. Pakadali pano ntchito yoyika magesi ili mugawo la nambala 8 ndipo gawo limeneli linayambidwa mu 2017 potelo kuti malo okwanila 452 anakidwa magetsi mu dziko lino. Koma poona kuti panalinso malo ambiri amene amafunika magetsi mwachangu, boma linaganiza zowonjezera malo oikidwa magetsi ndicholinga chofuna kuti magetsiwa afikire anthu ochuluka. Gawo loonjezerari lafikira

madera oposa 394 Dziko lonse lino. Pamodzi gawo la nambala 8 kuphatikiza ndiloonjezera laika magetsi madera 846 mu dziko lonse la Malawi. Ndipo mwamadera osewa kuno ku mpoto madera oposa 234 alandira magetsi. Mu boma lino lokha la Rumphi, madera okwanila 35 nawo alandila magetsi amenewa. Tili kuno ndi dera limodzi lamadera 35 amenewa.

Amayi ndi abambo izi zikuchitika kamba ka chidwi cha mtsogoleri wadziko lino professor Arthur Peter Mutharika yemwe akupereka ndalama zankhaninkhani ku ntchito imeneyi.

Amayi ndi Abambo, monga mukudziwa kuti magetsi ndi ofunikira kwambiri, boma pozindikira chimenechi, pano likupitiliza ntchito yopereka magetsi ndipo tsopano yilowa mu gawo la nambala 9. Ntchito yokozekera gawo limeneli ili mkati ndipo ntchito yomanga iyamba chaka chomwe chino. Gawo limeneli lithandizira kuti madera ochuluka kuno kumpoto komanso zigawo zonse alandire magetsi.

Izitu zikuchitika kamba kachidwi ndi mtima wachitukuko wa Mtsogoleri wadziko lino Professor Arthur Peter Mutharika ofuna kutukula miyoyo ya anthu akumidzi.

Amayi ndi Abambo, magetsi akafika pamalo amasintha miyoyo ya anthu munjira zosiyanasiyana. Tsopano kuno kwa Thazima ma bizinezi ofuna ma magesti monga zigayo ndi malo ootcherera zinthu azichitika komanso fanta kapena coca cola ozizira bwino azipezeka kuno, komanso anzathu ama bizinezi a babashopu, ma saluni ndi ena ambiri ofuna magetsi azitheka ndi magetsiwa.

Anyamata ndi asungwana asukulu nanunso tsopano maphuziro anu aziyenda bwino chifukwa muzikhala ndi nthawi yambiri yowerenga pogwiritsa ntchito magetsi.

Amayi ndi Abambo boma ndi Mtsogoleri wa dziko lino Professor Arthur Peter Mutharika likuzindikira kufunikira kwa magetsiku, ichitu ndi chifukwa chake Mtsogoleri wadziko lino akuonetsetsa kuti magetsiwa afika

kumadera akumidzi kuti anthu okhala m'madera amenewa nawonso azikhala moyo wapamwamba.

Amayi ndi Abambo, ndikuchenjezeni. Magetsitu ndi woopsya ngati sitisamala, choncho anthu akuno tiyeni titsate ndondomeko zoyenera kuti magetsiwa afike mnyumba zathu mwadongosolo kuti tipewe ngozi. Mukafuna magetsiwa pitani ku ESCOM ndipo iwowo mothandizana ndi boma akuthandizani moyenera kuti aliyense akhale ndi magetsi mnyumba mwake.

Amayi ndi Abambo, Mtsogoleri wa dziko lino Professor Arthur Peter Mutharika ndi boma akuyesetsa kuthandiza ndi ndalama zocholuka kuti ntchito imeneyi iziyenda bwino. Pachifukwa chimenechi ndikuthokoza Mtsogoleri wadziko linoyi ndikupemphanso kuti apitilize mtima wotukula a Malawi okhala kumidzi. Ichi ndi chifukwa chake ndikupempha inu abale anga muli pano tiyeni tisapote a Pulezidenti athu ndi boma lawo kuti ntchito yabwinoyi ipitilire.

Ndi mawu ochepa amenewa ndikulengeza kuti nthambo za magetsi za Thazima zayatsidwa lero pa 1st June, 2020.

***ZIKOMO MULUNGU AKUDALITSENI NONSE!!***